MAZIKO A BUKU LA GENESIS





“Pa tsiku lotsatira Yohane anaona Yesu akubwera kwa iye ndipo anati, “Taonani, Mwana Wankhosa wa Mulungu, amene achotsa tchimo la dziko lapansi!’ ”

Yohane 1:29

Baibulo linapangidwa ndi mabuku 66 olembedwa mosiyanasiyana, ndipo lidalembedwa ndi anthu opitilira 40 pazaka 1,500.

Tikhonza kuyembekezera kuti padzakhale kusiyana maganizo ndi kutsutsana pakati pa olembawo osiyanasiyana. Koma, tikamaphunzira Baibulo timapeza mgwirizano wathunthu. Kuphatikizapo, pali magawo a Baibulo amene sangathe kumvetsedwa popanda kufufuza m'magawo ena a Baibulo.

Tiphunzira mfundo imodzi yomasulira Malemba imene ingatithandize kudziwa tanthauzo la chizindikiro kapena fananizo, poyenda mu Baibulo lonse.



- Mfundo ya kutchulidwa koyamba.
- Genesis 22: Chikondi ndi Mwanawankhosa.
  - “amene MUMUKONDA”
  - “MWANAWANKHOSA ali kuti?”
- Genesis 2-3: Imfa ndi Njoka.
  - “MUDZAFA ndithu”
  - “NJOKA inali yochenjera kwambiri.”

MFUNDO YA KUTCHULIDWA KOYAMBA

"Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi kunthawi zonse" (Ahebri 13:8)

Maphunziro aliwonse amayamba ndi phunziro loyamba. Nthawi zambiri phunziro limeneli limafotokoza mfundo zimene zidzathandize kumvetsetsa bwino mutu weniweni maphunzirolo.


THE FIRST BOOK OF MOSES
CALLED
GENESIS*
CHAPTER 1
1 In the beginning God created the heaven and the earth.
2 And the earth was without form, and void; and darkness was upon the face of the deep. And the Spirit of God moved upon the face of the waters.
3 And God said, Let there be light: and there was light.
4 And God saw the light, that it was good: and God divided the light from the darkness.
5 And God called the light Day, and the darkness he called Night. And the evening and the morning were the first day.
6 And God said, Let there be a firmament in the midst of the waters, and let it divide the waters from the waters.
12 And the earth brought forth grass, and herb yielding seed after his kind, and the tree yielding fruit, whose seed was in itself, after his kind: and God saw that it was good.
13 And the evening and the morning were the third day.
14 And God said, Let there be lights in the firmament of the heaven to divide the day from the night; and let them be for signs, and for seasons, and for days, and years:
15 And let them be for lights in the firmament of the heaven to give light upon the earth: and it was so.
16 And God made two great lights; the greater light to rule the day, and the lesser light to rule the night: he made the stars also.
17 And God set them in the firmament of the heaven to give light upon the earth,
18 And to rule over the day and over the night, and to divide the light from the darkness: and God saw that it was good.

Mu Baibulo, timapeza "phunziro loyamba" limeneli m'buku la Genesis. Mmenemo, mawu ambiri ofunikira amaoneka koyamba, ndipo amatithandiza kumvetsa Dongosolo la Chipulumutso m'magawo onse a Baibulo.

Mulungu sasintha (Malachi 3:6a; Ahebri 13:8). Mawu ake nawonso sasintha (Yesaya 40:8). Choncho, palibe kutsutsana mu Baibulo. Dongosolo la chipulumutso limafotokozedwa pang'onopang'ono, kufikira limveke bwino — kapena lifike pamlingo womwe tifunikira kumvetsa panopa (2 Petro 1:19).

Tingamvetsetse bwino Yesu ndi zimene anatichitira ife pogwiritsa ntchito mfundo ya "kutchulidwa koyamba" m'buku la Genesis, pamene mawu ena ofunikira amawonekera koyamba: CHIKONDI, MWANAWANKHOSA, IMFA, ndi NJOKA.

GENESIS 22: CHIKONDI NDI MWANAWANKHOSA

“amene MUMUKONDA”

“Ndipo Mulungu anati, “Tenga Isake, mwana wako yekhayo amene umamukonda ndi kupita naye ku dziko la Moriya. Ukamupereke iye ngati nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri a kumeneko limene ndidzakuwuza” (Genesis 22:2)

Chikondi! Kodi tingafotokoze bwanji chikondi? Maganizo athu okhudza chikondi asokonezeka kwambiri chifukwa cha tchimo. Nanga tingamvetse bwanji chikondi cha Mulungu, chimene chiri choyera komanso chopatulika?

Kutchulidwa koyamba kwa chikondi mu Baibulo kumalankhula za ngwirizano wa pakati pa bambo ndi mwana wake: Abrahamu ndi Isake (Genesis 22:2). Tikayang’ana koyamba, nkhaniyi imawoneka yowopsa: Abrahamu anayenera kupereka mwana wake wokondedwa ngati nsembe! (Musade nkhawa, sanamupereke konse.)

Yerekezani mawu otchulidwa koyamba kumena za chikondi komwe timakumana nako mu Uthenga Wabwino : “Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa” (Mateyu 3:17; Marko 1:11; Luka 3:22.)

Ndipo tisaiwale kutchulidwa koyamba kwa chikondi mu buku la Yohane (Yohane 3:16). Zimene Abrahamu anachita popereka mwana wake monga nsembe zimasonyeza momwe Mulungu amatikondera, kufika popereka nsembe Mwana wake yekha kuti ife tikhale ndi moyo wosatha..

“MWANAWANKHOSA ali kuti?”

“Ndipo Isaki ananena ndi Abrahamu atate wake, nati, Atate wanga; ndipo iye anati, Ndine pano, mwana wanga. Ndipo anati, Taonani moto ndi nkhuni; koma mwanawankhosa wa nsembe yopsereza ali kuti?” (Genesis 22:7)

Kutchulidwa koyamba kwa mawu akuti MWANAWANKHOSA sikochitika mwangozi (Genesis 22:7). Ndi maziko omvetsetsa kutchulidwa mobwerezabwereza kwa Mwanawankhosa mu Chivumbulutso (Chiv. 5:6).

Dziwani kuti Mwanawankhosa amene Mulungu anapereka anali nkhosa yamphongo (Gen. 22:8, 13). Pa Phwando la Pasika, ankagwiritsa ntchito Mwanawankhosa ngati nsembe, gakhale zinali zotheka kugwiritsa ntchito mwana wa nkhosa kapena mwana wa mbuzi (Eksodo 12:3, 5). Izi zikutanthauza kuti mawu akuti “Mwanawankhosa” anayamba kutanthauza nsembe yayikulu. Pang’onopang’ono, Baibulo limakulitsa kuzindira kwa tanthauzo la chizindikiro cha Mwanawankhosa:

Iye analetsa imfa yamwana oyamba kubadwa (Eksodo 12:13)

Inali nsembe yomwe Mulungu ankaganizira kuyambira pa chiyambi (Eksodo 29:38-41)

Ndinkayenera kufa chifukwa cha machimo anga (Yesaya 53:6-8)

Yohane M’batizi anazindikira Mwanawankhosa (Yohane 1:29)

Ndizosadabwitsa kuti buku la Chivumbulutso silifotokoza kuti Mwanawankhosa ndi ndani. Mwanawankhosa ndi Yesu, amene anaperekedwa ngati nsembe chifukwa cha machimo anga, ndipo nthawi zonse amandipembedzera kwa Atate (Ahebri 7:25)

“Zinali zovuta ngakhale kwa angelo kumvetsetsa chinsinsi cha chiombolo—kumvetsa kuti Mkulu wa Nkhondo wa kumwamba, Mwana wa Mulungu, ayenera kufa chifukwa cha munthu wochimwa. Pamene lamulo linaperekedwa kwa Abrahamu kuti apereke mwana wake ngati nsembe, zolengedwa zonse zakumwamba zinachita chidwi. Ndi chidwi chachikulu, anatsatira ndondomeko iri yonse yochitika pokwaniritsa lamulo limeneli. Pamene Isake anafunsa kuti, “Koma mwana wa nkhosa wopereka nsembe ali kuti?” ndipo Abrahamu anayankha kuti, “Mulungu adzapereka yekha mwana wa nkhosa,”—ndipo pamene dzanja la abambo linayimitsidwa kuti lisanaphe mwana wake, ndipo Mulungu anapereka nkhosa yaimuna m'malo mwa Isake—pomwepo, kuwala kunayamba kuwunikira pa chinsinsi cha chiombolo, ndipo ngakhale angelo anayamba kumvetsa bwino kwambiri njira yodabwitsa imene Mulungu anakonza yopulumutsira munthu.”

EGW (Patriarchs and Prophets, pg. 155)

GENESIS 2-3: IMFA NDI NJOKA

“MUDZAFA ndithu”

“koma usadye zipatso za mu mtengo wodziwitsa chabwino ndi choyipa, popeza ukadzadya za mu mtengowu udzafa ndithu” (Genesis 2:17)



Mulungu anali woyamba kutchula za imfa (Genesis 2:17). Koma imfa imangoyenera kukhalapo monga chotsatira cha uchimo (Aroma 5:12)

Nthawi zambiri, imfa imalumikizidwa ndi ukalamba. Koma imfa yoyamba yolembedwa m’Baibulo inali ya mnyamata: Abele (Genesis 4:8). Iye, ngakhale anali munthu wolungama, anaphedwa ndi munthu wosalungama (Ahebri 11:4; 1 Yohane 3:12)



Mbiri inabwerezanso patatha zaka zambiri, pamene munthu Wolungama anaphedwa ndi anthu osalungama (Marko 15:14). Kusiyana ndi imfa ya Abele, Yesu akanatha kulepheletsa imfa yake—analola yekha kuti aphedwe (Aefeso 5:2)

Yesu anachita zomwe Abele sanaathe kuchita: Iye anagonjetsa imfa (Aroma 6:9). Ndipo monga momwe Chivumbulutso 1:18 imasonyezera, Yesu analandira “makiyi a imfa,” amene angatsegulire manda (“gehena” kapena “Hade”)

“NJOKA inali yochenjera kwambiri”

“Ndipo njoka inali yochenjera kuposa nyama yakuthengo iliyonse imene Yehova Mulungu anapanga” (Genesis 3:1a)

Buku la Chivumbulutso limatipatsa chithunzithunzi cha chinjoka (Chiv. 12:3-4). Limatiuzanso kuti chinjokachi ndi chizindikiro cha Satana (Chiv. 12:9)

Potizindikiritsa chizindikiro cha chinjokachi, Iye akuonjezeranso chizindikiro chatsopano: Satana ndi “chinjoka chakale.” Kodi chinjoka chomwe akutanthauza ndi chiti?

Nzachiziwikire, njoka yoyamba kutchulidwa mu Baibulo (Genesis 3:1). Mu Edeni, Satana (njoka) ananamizira dziko lonse lapansi (kuyimiliridwa ndi Adamu ndi Hava.

M’buku la Chivumbulutso, timakumbutsidwa kuti ichi chakhala cholinga cha Satana mu mbiri yonse, ndipo chidzakhala cholinga chake kumapeto kwa nthawi (Chiv. 13:14). Iye adzayesetsa kunamiza aliyense ngakhale ake a Mulungu mwini (Chiv. 20:8).

Kodi tingadziteteze bwanji ku chiwembu chake? Njira imodzi ndi kuphunzira momwe anayambira kuchitira zimenezi. Njira zake zofooketsa anthu sizinasinthe ngakhale papita zaka zambiri.

EGW (Manuscript) Releases, vol. 10, pg. 156)

“Uthenga Wabwino ukuwululidwa mu maulosi onse okhudza kubwera kwa Khristu koyamba monga Mpulumutsi wa anthu. Chochitika chirichonse mu chipangano chakale chowabweza anthu kuchokera ku uchimo ngakhalenso kuwakhululukira chinkachitika Poyang’ana Mpulumutsi yemwe amayembekezeredwa kubwera. Iye ndiye anali mwala wopondera kuti munthu uyenera kukwezedwa.”